# LESSON 30 YEMWE — YEMWE'YU

| | | | |
|---|---|---|---|
| **Bongo** | brain | **-vomera** | accept, agree |
| **Cholinga** | aim | **-khulupirira** | hope, believe |
| **Ganizo** | thought | **-ganiza** | think |
| **Maloto** | dream | **-lota** | dream |
| **Chizindikiro** | sign | **-zindikira** | recognize |
| **Msala** | madness | **-penga** | become mad |
| **Khunyu** | epilepsy | **-dabwa** | be astonished |
| **Chitsiru** | a fool | **-peneka** | doubt, hesitate |

YEMWE This word means "himself", or "the same", "even", "as well". The stem is -mwe; it also takes the Verbal adjective prefix **wo-**.

| | | | |
|---|---|---|---|
| 1 | **Ine** | **ndemwe** | Ine ndemwe **ndikuchita mantha.** I myself... |
| 2 | **Iwe** | **wemwe** | Iwe wemwe **umachita ulesi nthaŵi zina. Kodi si zoona?** |
| 3 | **Iye** | **yemwe** | Asatume mnzake, **koma abwere iye yemwe (: iye mwini).** |
| 1 | **Ife** | **tomwe** | **Ife tomwe tinapita kumsonkhano, chifukwa anatiitana.** |
| 2 | **Inu** | **nomwe** | Pepani **anzathu, musatiseke chifukwa inu nomwe mwalakwa.** |
| 3 | **Iwo** | **omwe** | **Akazi ao ali ndi usiŵa ndipo iwo omwe amavala nsanza** |

| | | | |
|---|---|---|---|
| 1 | **Yemwe** | **Omwe** | Anaba **ndalama zonse ndi katundu yemwe:** even |
| 2 | **Womwe** | **Yomwe** | **Tinatsiriza kubzala chimanga ndi mtedza womwe.** |
| 3 | **Chomwe** | **Zomwe** | **Anafentha nyumba,, nkhokwe ndi chimbudzi chomwe.** |
| 4 | **Yomwe** | **Zomwe** | **Anatenga katundu yense ndi mphasa yomwe.** |
| 5 | **Lomwe** | **Omwe** | **Werengani makwacha onse ndi matambbala omwe!** |
| 6 | **Womwe** | **Omwe** | **Ndinamweta tsekera ndi udzu womwe.** |
| D | **Komwe** | **Tomwe** | **Kambuku anapha mbuzi zonse ndi tiana tomwe.** |
| I | **Komwe** | | **Anaphunzira kuŵerenga ndi kulemba komwe.** |

It is often used as a Relative pronoun "the same... who": it puts more emphasis on the identity of the object, excluding any other.
**Mundipatse nyale yomwe iri apo!** more precise than **imene.**
**Nyumba yomwe khomo lake lilibe chitseko ndi yanga.**
**Mumpatse ndalama zomwe muli nazo! (: zimene muli nazo).**

Pomwe **Amakhala pa mudzi pomwe pali sukulu.** on the same spot where
**Ndinasesa mnyumba ndi pakhomo pomwe.** even

Komwe **Ndikukacheza kumudzi komwe kuli bwenzi langa.** where
**Tinakayenda ku Salima ndi kunyanja komwe.** even

Momwe **Anadzacheza mnyumba momwe timagona ife.** where
**Muyenera kusesa pakhomo ndi mnyumba momwe.** even

**Tsiku lomwe anathyoka mwendo tinapita naye kuchipatala.** the very day
**Nthaŵi yomwe tinatuluka msukulu mvula inayamba kugwa.** the same moment

...**ndi pang'ono pomwe** (with a negation) : not in the least.
**Alibe mantha ndi pang'ono pomwe. Sakumwa ndi pang'ono pomwe.**
**Sanaphunzire ndi pang'ono pomwe. Sanadye ndi pang'ono pomwe.**
**Ndiribe tambala ndi limodzi lomwe:** I don't have a single tambala
**Sanapite kwao ndi kamodzi komwe.**

Monga : **monga mmene: monga momwe:** as, like, in the same way that:
**Chitani monga momwe ndachitira ine.** Note suffix -ra p. 81
**Atsikana a panoŵa akubvina monga momwe timabvinira ife.**
**Kondani anzanu monga momwe ndinakukonderani.**

YEMWE'YU In this form of Demonstratives, the Relative **yemwe** followed by **uyu, uyo** or **uno, uja** re-inforces the identity of an object to the exclusion of any other. "this same...", "that same..."

| | | | |
|---|---|---|---|
| 1 | **Yemweyu** | **Omweŵa** | **Alibe katundu wina; ndi yemweyu (: yekhayu)** |
| 2 | **Womwewu** | **Yomweyi** | **Mkeka wanga ndi womwewu.** |
| 3 | **Chomwechi** | **Zomwezi** | **Cholinga changa ndi chomwechi.** |
| 4 | **Yemweyi** | **Zomwezi** | **Tenga nthochi yomweyi; zinazo zili zosapsya.** |
| 5 | **Lomweli** | **Omweŵa** | **Dzina langa lachikhristu ndi lomweli.** |
| 6 | **Womwewu** | **Omwewu** | **Ufa umene ndili nawo ndi womwewu: sukwanira.** |
| D | **Komweka** | **Tomweti** | **Kankhuku kaja kadasoŵa dzana ndi komweka.** |
| I | **Komweku** | | **Kulakwa kwanga ndi komweku.** |

| | |
|---|---|
| **Pomwepa** | **Khalani pomwepa, chifukwa palibe malo ena. (: pompa)** |
| **Komweku** | **Inunso kakhaleni ku mpanda komweku! (: konku)** |
| **Momwemu** | **Leronso tigona momwemu. (: mommu)** in this same house |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | **Yemweyo** | **Omwewo** | **Yemweuno** | **Omweano** | **Yemweuja** | **Omweaja ...** etc. |
| D | **Komweko** | **Tomweto** | **Komwekano** | **Tomwetino** | **Komwekaja** | **Tomwetija** |
| I | **Komweko** | | **Komwekuno** | | **Komwekuja** | |
| | **Pomwepo** | **(pompo)** | **Pomwepano** | **(pompano)** | **Pomwepaja** | **(pompaja)** |
| | **Komweko** | **(konko)** | **Komwekuno** | **(konkuno)** | **Komwekuja** | **(konkuja)** |
| | **Momwemo** | **(mommo)** | **Mamwemuno** | **(mommuno)** | **Momwemuja** | **(mommuja)** |

**Chomwechi (chonchi)** like this: **Gule ameneyu timavina chonchi.**
**Chomwecho (choncho)** like that: **Chitani choncho!**
**Choncho!** It is like that! Such is life! **Choncho! Titani nanga?**
**Mau anga ndi omwewo.** That is what I wanted to say. (closing a speech)
**Kudandaula kwanga ndi komweko. Kulakwa kwanu ndi komweko.**

Proverb: **Kulasa mtengo ndi chamuna chomwe.**